


KUWALA KWAKUKURU

 Phunziro langa mmawa uno likupezeke mu Chipangano Chatsopano. Poyamba pakhala kuwerenga kwa Malemba kuchokera mu Mateyu 1 . . . mutu wa 2, kuyambira ndime ya 1. Ndiyenso ine ndikufuna kutenga, monga phunziro, kuchokera mu mutu wa 4, ndipo ndime ya 14 ndi ya 15. Ine ndimakonda kuwerenga Mawu, chifukwa Mawu ndiwo Mulungu.

Tsopano pamene Yesu anabadwa m'Betelehemu wa Yudeya m'masiku a Herode mfumu, taonani, anadza anzeru a kum'mawa ku Yerusalemu,

Nanena, Ali kuti yemwe wabadwa ali Mfumu ya Ayuda? pakuti ife tinaona nyenyezi yache kum'mawa, ndipo tabwera kudzamlambira iye.

² Ndiye mu mutu wa 4 ndipo ndime ya 14, kulankhula zokhudza mneneri.

Kuti chikachitidwe chomwe chinanenedwa ndi Yesaya mneneri, kuti,

Dziko la Zebuloni ndi dziko la Nafitali, njira ya kunyanja, kutsidya la Yordano, Galileya wa a Amitundu;

Anthu omwe anakhala mu mdima anaona kuwala kwakukuru; ndipo kwa iwo amene anakhala mzigawo za mthunzi wa imfa kuwala kunawatulukira.

³ Ine ndikufuna kutenga phunziro langa kuchokera . . . monga ili: *Kuwala Kwakukuru*. Ndiro Lemba losazolowereka kwambiri.

⁴ Ndipo, pa nthawi iyi, anthu mwachizolowezi alalikira kwambiri pa “mulibe malo mnyumba ya alendo,” nyengo ya chisangalalo, ndiponso “Yosefe ndi Maria,” ndi—ndi “kubadwa kwa Ambuye Yesu.” Dzulo ine ndimaganiza kuti ine ndiyesa kufikapo mwanjira yosiyana, kuti ambiri ainu mumvere wailesi yanu ndi matelevizioni.

⁵ Ndipo ndiri chiganizire, ichi chinabwera mmalingaliro anga, za amagi ndi nyenyezi. Ndipo chomwe chinandikhudza ine chinali, chakuti, kodi amagi ali ndi chochita chanji naye Khristu? Chotero, powerenga zolemba zambiri za ophunzira akale, usiku wapitawu, mochedwa, mpaka ine ndinagona pa tebulo, kuyesa kupeza chinachake chimene chikanakhoza kubweretsa kuwala kochepe pa phunziro la lero.

⁶ Ndiye, ndi chinthu chosazolowereka kulankhula za zinthu izi, chifukwa, kuwonjezera apo, Mulungu ndi wosazolowereka. Mulungu amachita zinthu mwanjira yosazolowereka, ndipo nthawi zina pa nthawi yosazolowereka, chifukwa Iye ndi

wosazolowereka kwambiri. Ndipo iwo amene amamutumikira Iye ndi osazolowereka; iwo ndi anthu achirendo.

⁷ Kotero monga ife, nthawi iyi ya nyengo, pamene ife tikuyang'anitsa kuganiza kwathu cha ku Khristimasi, ndi zoyipa kwambiri kuti ife tiyiike iyo ku nthano yotchedwa "Santa Claus," m'malo mwa Khristimasi yeniyeni yomwe ikuyenera kukhalapo. Ana aang'ono ochuluka mdzikoli lero sadziwa china kuposa kuti Khristimasi imatanthawuza "ngolo yodzaza ndi zidole, ndi agwape ena amatsenga akugunda pa nyumba," kudzadziwa patsogolo chabe za nthano iyi; modzavulaza ngakhale chikhulupiriro chawo, pamene zifika podziwa nkhani yeniyeni ya Khristimasi, kuti inalibe chochita chirichonse ndi agwape, kapena munthu akusuta kaliwo, ndi ubweya wozungulira chikhotho chake.

⁸ Iko kunali kubadwa kwa Ambuye Yesu wathu wodala. Ndipo ndi chosazolowereka kwambiri kuwona momwe Mulungu anachitira motere, chifukwa palibe nthawi yina zikanagwira ntchito mu mbiriyakale yonse ya mdziko. Zinayenera kukhala mofanana kwenikweni pa nthawi ino. Ndipo tsopano kwa mphindi zochepa tiyeni tingoyang'ana pa nyengoyi.

⁹ Iyo inali nthawi yomwe Herode, wakupha, anali mfumu. Anayenera kukhala, munthu uyu wosaleza mtima anayenera kukhala mfumu pa nthawiyo, pakuti ife tikudziwa Malemba amene amati iye "anapha ana onse oyambira zaka ziwiri zakubadwa mpaka mmusi," kuyesa kuti ampeze Khristu. Ndipo zinayenera kukhala pa nthawi imeneyo basi.

¹⁰ Ndiyeno panayenera kukhala, pa nthawi, yomwe kukanakhala akukweza msonkho, kuti zimuchititse Maria ndi Yosefe kubwerera ku tawoni ya kwawo ya Betelehemu kumene iwo anali mu kaundula, ndipo kalemba anali mu zolembedwa za mmakhothi ndi mkachisi, kuti akakhometsedwe msonkho. Ndipo Khristu anali woti akabadwire mu Betelehemu, ndipo iwo anali mamailosi ochuluka kutali pamene izi zinkachitika.

¹¹ Ndipo ife taona zowopsya zomwe iwo anapolyamo, ndi cholinga chakuti akafike kumeneko. Tsopano iwo analibe ambulasi yopambana, yomangidwa bwino kuti amutengeremo Maria kumeneko. Ndipo iwo analibe iyo monga lero, kuti ife mwina tingakhale ndi chowiringula cha mtundu wina. Ilo linali lamulo la mfumu. Palibe zowiringula zomwe zipangidwe. Izo zinayenera kukwaniritsidwa. "Mfumu inatero!" Ziribe kanthu mmene iye analiri, kapena chiyani, iwo ayenera kubwerera ku dziko la kwawo. Panalibe zawofuwofu kwa mayi wamng'ono woyembekezerayu. Ndipo panalibe kayendedwe kena; wombambanda basi, kapena pa msana wa bulu wamng'ono.

¹² Ndipo ife tawuzidwa kuti Yosefe anamutenga Maria, mayi uyu woyembekezera nthawi iliyonse, ndi kumukhazika iye

pa msana pa bulu wamng'ono. Ndipo ngati wina aliyense anakwerapo bulu, akudziwa mabampu ake ndi otani. Kamunthu kakang'ono, kakuyenda mu kanjira kakang'ono kokhotakhota kopyola mmapiri, kubwera ku Betelehemu, kuchokera kumusi kwa Yudea, msewu woyipa ndi wokumbika. Nanga bwanji ngati buluyo akadakhala kuti mapazi ake ndi osadalirika, ndipo akanagwa ndi mayi wamng'ono woyembekezerayu?

¹³ Kapena, mmasiku pamene kunali kuyenda kochuluka kubwera ku maiko a kwawo, dziko lonse limagwira ntchito, kutanganidwa ndi ogonera ndi oyenda, kubwera ku dziko la kwawo, dongosolo la bwino kwa achifwamba mmasiku amenewo. Pamene iwo awona magulu ochepa a anthu a magareta; okwera, akuba akanakhoza kukweramo ndi kuwapha iwo, ndikuwalanda akatundu awo nathawa. Chinali chinthu chotani kwa anthu awiri awa ongokwatirana kumene, chimene iwo akanakumana nacho, ndipo momwe zikanadzakhallira.

¹⁴ Ndiponso, bwanji ngati zina za zinyama zolusa, zomwe uko kunali mikango ndi zambiri zowononga, zinyama zolusa zimene zimayendayenda mu zipululu zomwe iwo amadutsamo. Bwanji ngati chirombo cholusa chikanamapita chaku kagulu kakang'onoko, Yosefe akanachita chiyani ndi ndodo mdzanja lake, ndi mkazi amene samakhoza kuyenda nkomwe? Iwo anali oti akumane ndi zimenezo.

¹⁵ Koma izo zimatipatsa ife chithoncho kudziwa ichi, kuti ife tiribe ulamuliro wa kumene tikupita. Mulungu akudziwa kumene tikupita. Ndipo Iye anakonza izo kuti zikhale choncho, ndipo palibe chirichonse chimene chiti chidzasokoneze dongosolo la Mulungu. Ife tiri okakamizidwa kukafikabe.

¹⁶ Ndipo apo sipanayenere kukhala mantha. Komabe mwina Maria ndi Yosefe, iwoeni, anthu wamba chabe, osaphunzira. Ndipo iwo analibe njira yodziwira zinthu izi, zimene zinkachitika pa nthawi imeneyo, kunali kukwaniritisa Malemba.

¹⁷ Ndipo ndi chimodzimodzi lero. Zinthu zimene zikuchitika mtsiku lino limene ife tikukhalamo, ndipo ambiri aife sitikudziwa kanthu za izo, momwe Mulungu akuyendera.

¹⁸ Ine ndinangofunsidwa ndi mmodzi wa akazi ojambula mu chipinda kuno, kuti ndi liti pamene ndidzalankhule pa phunziro lija, la cholembedwa, ndi sputnik mu mlengalenga. “Kodi lidzakhala Lamlungu likudzali?”

Ine ndinati, “Ine sindikudziwa.”

¹⁹ Koma, o, kuwona mu nthawi iyi ya mdima wokuta ponseponse, dzanja lalikululu la Mulungu likuyenda modekha kumka patsogolo. Palibe chomwe chidzaliyimitse Ilo.

²⁰ Ndipo ife tikhoza kuwona monga izo zinaliri, lero, pomwe bulu wamng'onoyo ndi oyenda awiriwo potsiriza anafika. Pamene iwo anali kubwera ndi usiku, mu zipululu, kumatentha

kwambiri! Ndiyeno tiyeni tinene kuti iwo akhala pa phiri laling'ono kummawa kwa Betelehemu.

²¹ Betelehemu ali mu chigwa, ndipo muli kaphiri kakang'ono. Ndipo msewu umene umalowa mu Betelehemu, umakhota chakummawa kwa Betelehemu, nulowa mu mzindawo. Pafupi ndi kona, pamene inu mumakhota kotsiriza, kuti muyambe kutsika chitundacho, pali mulu wawukulu wa miyala yowonekera yomwe ili pamenepo. Ndipo zaganizidwa ndi a za mbiriyakale kuti mwina Maria ndi Yosefe anayima pamenepo kuti akoke mpweya pang'ono iwo asanatsikire mu mzindawo usiku umenewo.

²² Tiyeni timuwone Yosefe, mu kagwiridwe kache kosamalitsa, kumunyamula mkwatibwi wake wamng'ono kuchoka pa bulu ndi kumuthandizira iye kutsika, kumutenga iye mpaka kukamukhazika iye pa mwala, nati, “Wokonedwa, ndi uwo mzinda wawung'onowo, mmusi mwathumu basi, kumene mwina mulendo wathu wamng'ono akabadwireko.”

²³ Ine ndikhoza kulingalira powona nyenyezi zikungothwanima pang'ono ndikuwala, pomwe iwo anakhala akuyang'ana Betelehemu, cha kwao...chakummawa kwa iwo. Ndipo iwo pamene ali chikhalire pamenepo, akudabwa pamene iwo ankayang'ana nyenyezi; kutali, mamailosi mazana kummawa kwa pamenepo, kunali chowoneka china chikuyamba kuchitika.

²⁴ Inu mukudziwa, Mulungu amagwira ntchito mu chiregedwe Chake. Iye amapangitsa zinthu kuchitika mdziko limodzi, kumene Iye akuchipanga icho kuwoneka bwino kuti chikakumane mu chinzake. Uko ife tikuona, kutali chakummawa, monga tauzidwa ndi olemba mbiriyakale ambiri, kuti anthu awa, amagi, monga ife timawadziwira iwo kuti anali.

²⁵ Lero iwo akhoza kukhala, mochuluka kapena pang'ono, kutchedwa “akasidi,” osati mwa ganizo la a m'bwebwe; koma pali akasidi onamizira, omwe amatchedwa a m'bwebwe. Ndipo anthu amathamangira ku zinthu zimenezozomwe, zomwe ziri kwenikweni lingaliro lonama la mkasidi weniweni.

²⁶ Hampton anatiuza ife, wa za mbiriyakale wotchuka, kuti anali...Iwo anali Amedi-o-Persia, akasidi amenewa. Tiyeni tifufuze moyo wawo pang'ono pokha. Ndipo ife tikupeza kuti Amedi-o-Persia anawudziwa Uthenga wa Ambuye wathu ali ku Babeloni. Zaka za m'mbuyo, mu nthawi ya Mfumu Nebuchadnezzar, iwo anali nawo anthu monga akasidi, amene amayang'ana nyenyezi ndi matupi a mu mlengalenga. Ndipo iwo amakhoza kudziwa mwa zizindikiro ndi mayendedwe a nyenyezi, za zochitika zina zoti zichitika.

²⁷ Ndipo mafumu a masiku oyambirira amawafunsa anthu monga amenewa kuti adziwe zochitika ndi zinthu zomwe zinkati zidzachitike. Mulungu nthawizonse amafotokoza izo

mwa matupi Ake a m'wamba Iye asanazizindikiritse izo kwa dziko lapansi. Mulungu amalemba izo mmiyamba.

²⁸ Ndipo nyenyezi yomwe ife timayang'ana pa iyo, ndipo ife timaganiza za izo monga kagulu ka zinthu za makona asanu mmiyamba, koma, chomwe izo ziri, izo ndizo mayiko akulu kwambiri kuposa ili, akunyezimiritsa kuwala kwa dzuwa.

²⁹ Ndipo anthu amenewa zedi anawudziwa Uthenga mzaka za ukapolo wa Israeli, wa zaka 70 mdziko la Akaldia, ndipo, zedi, Danieli pokhala anapangidwa kukhala mkulu wa amagi. Mneneri, mwa nzeru zake zopambana kudziwa matsiriziro a zinthu, ndi kudziwa chimene Mulungu ati adzachite, ndipo iye anatchedwa mfumu ya amagi. Ndipo amagi anali ndi zolemba zakale zomwe iwo amafanizira kwa izo, za makolo awo akale. Ndipo Danieli anabweretsamo zolemba za Ambuye.

³⁰ Ndipo potero ife tikumvetsa kuti panthawi iyi iwo anali atachitira upo palimodzi mokwanira, ndipo iwo anali atawona luntha ndi mphamvu yomwe Mulungu mmodzi woona amawonetsa, yomwe inali yapamwamba kuposa mkasidi aliyense kapena m'magi. Izo zinatsimikiziridwa mu usiku wa Mfumu Nebuchadnezzar... kapena kuvina kwa Belteshazzar, kuti, palibe aliyense wa Akaldia kapena akasidi akanakhoza kuwerenga cholembedwa pa khoma. Koma Danieli, kupyolera mu Mzimu ndi mphamvu ya Mulungu wamoyo, akanakhoza kuchita izo. Ndipo zolemba zake zinasungidwa mopatulika, ndipo zikanalipobe mpaka lero lino.

³¹ Tsopano ife timawatcha iwo, ku mmawa... ine ndinali nawo mwayi wolankhula nawo iwo mu India. Ndipo iwo tsopano akutchedwa Achimuhamedi. Koma iwo kwenikweni anali Amedi-o-Persia. Amwenye amatchedwa... ine ndikukhulupirira iwo amawatcha iwo odetsedwa. Ndipo Amedi-o-Persia kwenikweni ndiwo Achimuhamedi. Ndipo iwo ndiwo amene anali ndi Mfumu Nebuchadnezzar pachiyambi. Ndipo aluntha awo opambana anali ophunzira amene amaphunzira—zinthu zachiregedwe, kuti afotokoze zinthu zauzimu zomwe zinali zoti zichitike.

³² Kotero mu zaka mazana zazitali izi, ndipo zolemba za kuphunzitsa kwa Danieli, ndi zina zotero, iwo anali atazisunga izo.

³³ Ndipo chimene iwo amachita, mu nthawi zoyambirira za madzulo, iwo amakhoza kukwera mu Assay[?] Mapiri. Ndipo kumeneko pamwamba apa iwo anali ndi linga. Ndipo mu linga ili munali linga la amagi. Ndipo iwo amakhala ndi phwando lawo la fujadous[?]. Ndipo likatha phwandolo iwo amatulukira pa madenga, kapena pa bwalo, ndipo kumeneko ku msanja yoyang'anira pamene dzuwa limakhala litalowa. Ndipo monga Achimuhamedi nthawizonse amachitira, kugwadira dzuwa nafaula, "Allah! Allah!" Ndipo nthawi zambiri kumadzidalitsa

okha ndi madzi opatulika, ndi zina zotero, ngakhale mpaka lero. Kambiri, chinthu chawo chopatulika kwambiri, chinali moto. Iwo amakhulupirira kuti Mulungu mmodzi woonayu amakhala mu moto.

³⁴ Ndipo ndi zodabwitsa chotani kudziwa kuti Mulungu mmodzi wona ndi wamoyo amakhala mu Kuwala, ndipo Iye ali Moto wonyeketsa.

³⁵ Momwe iwo amayatsira moto wopatulika! Ndipo iwo ankawuyang'ana moto uwu, chifukwa iwo amakhulupirira kuti Mulungu mmodzi wona ankakhala mmoto uwu, ndipo Iye amazinyezimiritsa Iyeyekha kwa iwo. Ndipo moto un kayaka kwambiri pamene ku—kuwala kwa dzuwa kunali kotalowa.

³⁶ Ndipo kotero iwo amakhoza kutulukira pa msanja iyi yoyang'anirapo, ndipo iwo amakhoza kuyang'ana mmwamba. Ndipo iwo anali ophunzitsidwa bwino. Ndipo iwo amadziwa kuyenda kulikonse kwa khamu lalikulu la nyenyezi za mmwamba. Iwo ankayang'anira mwatcheru kusuntha kulikonse.

³⁷ O, ngati Akhristu atamangochita zimenezo! Osati kuyang'ana nyenyezi, koma kuyang'ana Mawu a Mulungu pamene Iwo akuwululika. Ngati ife titangomazindikira zimenezo lero, ndikuona momwe Mulungu walonjezera mu tsiku ili zinthu zimene ife tikuyima nazo mwamphamvu. Mulungu walonjeza kuchita zinthu zimenezi, monga kuchiritsa odwala ndi kuchita zozizwitsa zazikulu.

³⁸ Danieli yemweyo amene anawaphunzitsa iwo za zochitika, ananena, kuti, “Mmasiku otsiriza anthu omwe adzadziwe Mulungu wao adzachita zambiri.” Malemba amenewo ayenera kukwaniritsidwa. Ngati ife tikanangofufuza! Ndipo ngati inu mungazindikire, Mulungu amangodziulula Iyemwini kwa iwo amene akufufuza ndi kukhumba kumuona Iye. “Yandikirani kwa Ine, ndipo Ine ndidzayandikira kwa inu,” atero Ambuye. Ndipo nthawizina Mulungu amalola zinthu zichitike kuti ife tiyandikire pafupi kwa Iye. Pakuti Mulungu zedi wayika kuti zochitika zina zichitike, ndipo izo zidzaululika pamene nthawi ya koloko Yake yamphamvu ifika pa zimenezo.

³⁹ Ndipo apo, ife titi, usiku wina, phwando litatha kale, ndipo iwo atagwadira kulowa kwa dzuwa, gulu lathu limakwera mpaka mu msanja iyi yoyang'anirapo. Ndipo pamene matupi opambana akumwamba ayamba kuwonekera mu mlengalenga, zolembe zakalekale zija, za aluntha, zimaturutsidwa. Ndipo zimafunyululidwa, ndipo iwo amayang'ana mmenemo, ndipo iwo amati, o, zinthu zina zimene zinaloseredwa. Ndipo phunziro lake, mwina, limapita nthawi yayitali, ya kugwa kwakukulu kwa maufumu, ndi kulephera kuyima kwa maufumu awo akulu, ndiponso momwe makhalidwe a miyoyo ya anthu, ndi nkondo, omwe anawononga dziko ndi kulisambitsa ilo ndi

magazi a abwenzi awo. Ndipo monga anthu omwe ali auzimu amamvetsa zinthu zauzimu zokhazo; momwe kukwaniritsika kwa masiku opambana amene apita, ndi manyazi awo, monga moto wopatulika unkayakira mpaka mumlengalenga niuzima, kuyimira Mulungu mmodzi woona ndi wamoyo.

⁴⁰ Ndipo pamene m'dima unafika ku gawo lake lapakati, titi, 10 koloko kapena 11, pamene khamu linali litakhala pamenepo, mwina likuyimba nyimbo zake, kapena mwina iwo anali akupemphera. Ife sitikudziwa chimene iwo anali akuchita, ndipo aza mbiriyakale samalankhula momveka pamenepo. Koma, ngakhalebe, iwo ayenera kuti anali mu lingaliro lauzimu, pakuti Mulungu amapembedza pamene pali umodzi ndi mzimu.

⁴¹ Mulungu abwera kwa ife mmawa uno. Iye apulumutsa moyo wa msungwana wokonedwa wamng'onoyu, ndi ambiri ainu muno amene mwina akufa ndi khansara ndiponso ndi matenda ena, ngati ife titangolowa mu umodzi wa mzimu ndi Mawu Ake ndiponso ndi Iye. Mulungu adzadzilula Iyemwini. Iye nthawizonse amachita zimenezo.

⁴² Pa njira ya ku Emau, chitatha chiukitsiro, zinali chabe pamene Teofilo ndi mzake anayamba kulankhula kwa Iye, ndipo Malemba anatchulidwa, ndipo Mulungu mwa Khristu anadziulula Iyemwini kwa iwo. Ndiyeno paulendo wobwerera, iwo anati, “Kodi mitima yathu siyinatenthe mkati mwathu pamene ife timalankhula ndi Iye mu msewu?” Chinachake cha kulankhula za Mawu!

⁴³ Ndipo mu zolemba zawo zakale, pamene iwo ankawerenga za amagi osiyanasiyana amene anafa. Ndipo ine sindingathe kulitchula Baibulo lawo pa nthawi iyi, kapena iwo analitcha Zedakoah[?], chinachake mwa njira imeneyo, limene iwo ankawerenga nafanizira ku zolemba izi za munthu wawo wopatulika. Ndipo momwe ambiri aiwo anali opembedza mafano, ndipo anabweretsa manyazi ndi chitonzo kwa anthu, nzosakayikitsa kuti amagi awa ankaweramitsa mitu yawo mwamanyazi. Komabe, ndiye moto wopatulika woyaka, umayimira Mulungu woona.

⁴⁴ Ndiye ine ndikukhoza kuwaona akubwera kuchokera ku linga, wina ali ndi mpukutu mdzanja lake. Ndipo iye akuwupereka iwo kwa aluntha iwo alichikhalire pa msanja yoyang'anirapo, akuyang'ana nyenyezi, ndipo chirichonse chikusuntha mwangwiro mwa chigwirizano, monga izo zinkachitira usiku ndi usiku, monga Mulungu anakonzera izo.

⁴⁵ Ndipo mkati umu, pamene iwo akulankhula za maufumu kugwa, iwo anawerenga gawo la Danieli, lomwe linati, “Ine ndinapenya kufikira mwala unasemedwa kuchokera ku phiri, popanda manja, ndipo iwo unaphwanya maufumu a mdziko ndipo iwo anasandulika ngati-ngati mungu pa dwale lopunthira. Ndipo mwala uwu waukulu unakula kukhala phiri

lomwe linaphimba dziko lonse. Ndipo ufumu Wake udzakhala ufumu wa nthawi za nthawi.” Chiyembekezo chawo pamenepo chinayatsidwa mpaka nthawi yomwe maufumu adzathere kugwa, ndipo pamene maufumu adzathere kuwonongedwa, pakuti kunali kudza ufumu wa nthawi zonse woyikidwa ndi Mulungu mmodzi woona ndi wamoyo.

⁴⁶ Ndipo pamene iwo ankalingalira pa zinthu zimenezi, pa Malemba, wina ayenera kuti anayang’ana m’mwamba. Ndipo apo panali mlendo pakati pawo. Iwo anawona Kuwala kumene iwo anali asanakuwone ndi kale lomwe. Iyo inali Nyenyezi ya chifumu imene inali isanakhalepo, mpaka nthawi iyi, kukhalapo, kapena siyinawonekerepo kwa maso amagi. Koma apo iyo inali. Bwanji? Malemba ayenera kukwaniritsidwa.

⁴⁷ Inu mukuti, ndiye, “M’bale Branham, kodi inu mukuganiza kuti Mulungu akanachita ndi amagi amenewo?”

⁴⁸ Baibulo linati, mu Aheberi mutu wa 1 ndi ndime ya 1, kuti, “Mulungu, nthawi zakale, mmanenedwe osiyana,” mmanenedwe a mitundu ina yonse, “Iye analankhula kwa makolo.”

⁴⁹ Izo zalembedwanso mu Machitidwe 10:35, kuti, “Mulungu salemekeza munthu, koma Iye amachitira ulemu iwo, mu fuko lirilonse, amene akukhumba kumutumikira Iye mu chirungamo.” Ngakhale iwe ukhale mu kulakwitsa, komabe, mu chirungamo cha—cha kuwonetsera kwa mtima wako kuti iwe ukufuna kutumikira Mulungu, Mulungu adzalemekeza chimenecho. Choncho, potero zipembedzo ziribe malire amene izo zingakhoze kuyika, amene ati adzamuyimike Mulungu ku nthano iliyonse, chifukwa Mulungu adzayang’ana pa zolinga za mtima wa munthu, ndipo pamenepo Iye adzagwira ntchito kuchokera pamalo amenewo.

⁵⁰ Ndipo ife tikupeza kuti amagi amenewa, woona mu mtima mwao ndikukhumba kuti awone Mulungu mmodzi woonayo, ndi kuyang’anira ulosi Wake kuti ukwaniritsidwe, umene unanena kuti, “Ambuye adzamuukitsa Iye ndi kupanga. . . ufumu Wake udzakhala wopanda matsiriziro. Iwo udzakhala ufumu wa nthawizonse.”

⁵¹ Panali pa nthawi imeneyo pomwe Nyenyezi, yomwe ife tikuyidziwa lero potchedwa Nyenyezi, inawonekera mu mlengalenga. Ine ndikhoza kulingalira kuti amagi amenewo, ndi umodzi wachigwirizano, anayima kakasi pamene iwo ankayang’ana kupambana kwa Nyenyezi yomwe inaphwanya malamulo a zothandizira dzuwa, ndipo inali itachoka ku kuwundana kwakukulu kwa matupi a mmwamba, kuwonetsera chinachake pamene icho chikukonzekera kuchitika.

⁵² Ine ndikuyembekeza pa mfundo iyi inu mukhoza kuwerenga pakati pa mizere ndi kudziwa chomwe ife tikutanthawuza, kuti mtsiku lino, Mulungu wanyoza chirichonse, kudzadziwonetsera Iyemwini, kuti Iye ali moyo lero, wauka kwa akufa, mu Thupi

Lake lopambana lakumwamba. Chithunzi pano cha Umunthu Wake chikhoza kunyoza wosapembedza aliyense mdziko. Iye ali moyo kwa nthawizonse. Mulungu amachita zinthu mwa njira Yake Yake, yachirendo.

⁵³ Koma, iwo anali atayang'ana kuwala kwa mmwamba, koma Kuwala uku kumawoneka kosiyana ndi kwina konseko.

⁵⁴ Ndipo ife tapenya, lero, zowala mu mpingo. Ife tawaona a Methodisiti, a Baptisti, a Chipentekoste, a Chipresbateria, zowala.

⁵⁵ Koma kwa iwo amene akumuyang'anira Iye, kukuwoneka kuti pali Kuwala kosiyana komwe kwayamba kuwala, komwe kukumuwonetsera Iye. "Iye ali yemweyo dzulo, lero, ndi nthawizonse." Mu kukongola Kwake kopambana ndi mphamvu, kwa Thupi la mmwamba limene latumizidwa mwa maonekedwe a Mzimu Woyera, mu masiku ano otsiriza kwa Mpingo, kuti awonetsere mphamvu Yake ya chiukitsiro, ndipo Iye ali kwa nthawizonse Kuwala Kwamuyaya kumene tsopano kukupezeka pakati pa Okhulupirira Ake. O, ndi chopambana motani kuti tiwone chimene Iye amachita!

⁵⁶ Ndipo pamenepo iwo ali chiyimire, opanda cholankhula, wina sakanatha kulankhula kwa mzake, pakuti ulemerero wa Kuwala uku unawasiya iwo opanda cholankhula.

⁵⁷ O, momwe ziri lero, mzanga wosauka wofooka, kuti pamene munthu amene sanadziwepo Mphamvu Yake, kuti apereke Kuwala kwatsopano ndikupereka chiyembekezo chatsopano, pamene iye ayenda mpaka Pamaso pa Umunthu Wauzimu wa Khristu, ndi chikhulupiriro chimene chimampangitsa iye chidwi kukhala opanda cholankhula kwa ukulu Wake. Siziri ngati kupita ku guwa ndikumpatsa mtumiki dzanja lanu lamanja, sizirinso ngati kupita mu dziwe kuti mukabatizidwe, kapena kuyima ndi chigoba kuti mukonkhedwe. Ndi kulowa mu Kuwala kumene inu simunayambe mwakuwonapo kale. Ndi nangula wa chikhulupiriro Chauzimu chomwe chimatcha chirichonse chosiyana ndi Mawu a Mulungu ngati kuti panalibe. Icho chimayika Moyo watsopano. Icho chimapereka chiyembekezo kwa akufa. Icho chimapereka chirimbikitso kwa ofooka. Icho chimapereka machiritso kwa odwala. Icho chimapereka madalitso kwa osakonedwa. Ndi chodabwitsa chotani kulowa mu Kuwala kwa Kukhalapo Kwake! Osati nthano. Singatinso chinachake chomwe winawake alinacho mwathupi, mmalingaliro ake, atachijambula. Koma, ndi kubwera molunjika mu Kukhalapo kwa Mfumu ya Ulemerero, Kuwala Kwamuyaya kwa Mulungu wamoyo.

⁵⁸ Pamene chinachake chichitika, chimene chimazika chiyembekezocho mwa inu, mwakuti ziribe kanthu kaya mudwala chotani, pambuyo pake, ndi mwamtheradi kuti sikwabwino kuti Mdierekezi ayesere kukuyesani inu ndi

chirichonse chosiyana. Icho chakhazikika kwa nthawizonse. Ziribe kanthu mdani ayesere chotani kukupangani inu kuyesa kukhala moyo wolakwika, inu mwazikika kwa nthawizonse, pakuti inu mwalowa mu Kukhalapo Kwake, mu Kuwala Kwauzimu komwe kwasintha munthu wamkati wanu ndi kuyikamo chisangalalo, belu la chipulumutso, likulira mu mtima wanu, mwakuti dziko silikudziwa kanthu za, kuti inu mwachoka ku imfa kulowa mu Moyo. Imfa ndi mithunzi yake yathawa kwa inu, ndipo inu mwakhala cholengedwa chatsopano pamene inu mulowa mu Kuwala Kwauzimu uku.

⁵⁹ Monga amagi aja anayima, kusowa cholankhula, pamene iwo ankayang'ana Kuwala kumeneko, potsiriza ine ndikukhoza kumva wina akunena kwa mzake, "O, kodi ichi si chizindikiro chopambana kuti chinachake chiri pafupi kuchitika!"

⁶⁰ Zedi, lero, naponso, pamene ife tilowa mu Kukhalapo kwa Ambuye Yesu, ndi chizindikiro Chauzimu kuti chinachake chiri pafupi kuchitika; Kudza kwachiwiri kwa ulemerero Wake kwayandikira.

⁶¹ Ndipo pamene iwo anayang'anana, wina kwa mzake, ndipo patapita kamphindi. . . Iwo anayipenya Iyo, mwina, usiku wonse. Momwe Iyo imanyezimirira! Iyo imawoneka yowala kuposa nyenyezi zina. Iyo imawoneka ngati kuti iwo sakanatha kuchotsa maso awo pa Iyo, kuti ayang'ane pa nyenyezi yina iliyonse.

⁶² Ndipo ine ndikutsimikiza, ngati ife tiwona Kuwala kopambana Kwamuyayako kukuwalira pa nkhope yathu, ife sitidzayang'ana pa zipembedzo zathu, ndi kunena, "Ife ndife Abaptisti, kapena ndife Apresbateria, kapena ndife a Chipentekoste," kapena chirichonse chimene chikhoza kukhala. Ife timangoyang'ana ku Kuwala, ndi kukhala moyo. Iye ndiye Zowala Zamuyaya.

⁶³ Ndipo pamene iwo ankayiyang'ana Iyo, pamene potsiriza dzuwa linatuluka. . . Masana onse iwo amagona. Ine ndawawonapo iwo atakhala mmisewu ku India, atapingasitsa miyendo yawo, mitu yawo palimodzi; popeza iwo nthawi ya masana amagona, ndipo nthawi ya usiku iwo amapita kukayang'ana nyenyezi, kuyang'anira kusuntha kulikonse.

⁶⁴ Ndi okhawo amene akumuyembekezera Iye amene adzamuwone Iye. Ndi okhawo amene akukhulupirira mwa Iye ati adzamve bwino madalitso Ake. Ndi okhawo amene amakhulupirira machiritso ati adzalandire machiritso. Ndi okhawo omwe akhulupirira chipulumutso amene ati adzachipeze icho. Zinthu zonse ndi zotheka kwa iwo amene akhulupirira. Koma, poyamba, lisangokhala ganizo lojambulidwa mwachithupi. Ilo liyenera kukhala vumbulutso lolunjika lotumizidwa kuchokera kwa Mulungu yekha, ndipo pamene ife tikuyembekezera.

⁶⁵ Ife tikupeza, usiku ndi usiku, iwo ankayiyang'ana Iyo. Iwo amakambirana za Iyo. Iwo amayang'ana pa Malemba, ndipo ali nkufufuza. Ine ndikhoza kuwona mmodzi akubwera, nati, "Pano pali cholembedwa china cha Chihebri. Ichu chikuchokera kwa mmodzi wa aneneri awo, dzina lake Balaamu. Ndipo iye anati, 'Kudzatuluka nyenyezi kwa Yakobo.'" Ndipo iwo anawona Malemba akukwaniritsidwa. O, momwe mitima yawo inasangalalira!

⁶⁶ Ndipo momwe izo ziyenera kupanga mitima yathu kusangalala, kudziwa kuti mu tsiku ili loyipa limene ife tsopano tikukhalamo, kumawona Zolembedwa zoyera za Mulungu zikukwaniritsidwa ndi kuwululidwa kwa ife ngati Kuwala kopambana kofufuza mu umunthu wathu.

⁶⁷ Ndiye, patapita kanthawi, pamene iwo ankayipenya Iyo, modabwitsa usiku wina Iyo inayamba kusuntha. Ndipo ife nthawizonse timasuntha limodzi ndi Kuwala. Ndipo Kuwalako kunayamba kusunthira chakumadzulo. Mofulumira iwo anapachira ngamira zawo ndi zaulemu zawo zonse. Iwo anatenga mphatso. Ndipo ine ndikukhoza kuwawona iwo pamene akuyamba ulendo wawo, kutsatira Kuwala, pakuti iwo amaziziwa kuti chinali Chinthu chakumwamba. Iyo inayenera kunyezimiritsa Kuwala kwina kopambana.

⁶⁸ Chimodzimodzinsu lero, mzanga, pamene ife tiwona nyenyezi ikuwala, ife tikudziwa kuti ndi chinyezimiritsa cha dzuwa. Pamene ife tiwona mwezi ukuwala, ife timadziwa kuti ndi chinyezimiritsa cha kuwala kopambana.

⁶⁹ Pamene ife tiwona mpingo ukuwala, ife timadziwa kuti ndi chinyezimiritsa cha Kuwala kopambana, Kuwala kopanda chivundi ndi Kwamuyaya. Koma pamene ife tidziphimba tokha, ndi kutembenuza mitima yathu, ndi kutembenezira chikhulupiriro chatu kwina, ndi kuti, "Masiku a zodabwitsa anapita, ndipo palibenso zinthu zonga ngati izi ayinso," ife tikutembenezira misana yathu ku Kuwala Kwamuyaya kwa Mulungu.

⁷⁰ Ndipo pamene iwo anali chiyendere, ine ndikukhoza kuwawona iwo akusiya mapiri napita ku matsitso a kumadzulo. Iwo amatsata matsitso mpaka ku Mtsinje wa Tigrisi, ndipo kumeneko iwo anatsatira Tigrisi wopambana kutsikira mmusi mpaka iwo analowa mu Babeloni, anawoloka doko la Efurate, mpaka mmusi, nazungulira mayiko a Palestina. Akusangalala! Iwo ankayenda ndi usiku chifukwa kunali kuzizirirako usiku, kuti iwo ayende kupyola mzipululu. Chinthu china chinali, nyenyezi zimawala mu mdima, kotero iwo amayenera kutsatira Kuwalako. Ndipo Kuwala kunali namulondola wawo.

⁷¹ Ndipo pamene iwo anali kubwera, potsiriza Iyo inafika ku Yerusalemu. Koma, pamene Iyo inafika mu Yerusalemu, Iyo inazima. Iyo mwadzidzidzi inasowa pamene iwo anafika mu

Yerusalemu, chifukwa inali nthawi yawo tsopano yowonetsa Kuwalako.

⁷² Ndipo akuyenda kudzera mmisewu yokhota ya mu mzinda wawukuluwo, akuyenda kudzera mmisewu ya likulu lakale la dziko lapansi, pafupifupi, Yerusalemu; kokhala kwa nthawi imodzi kwa Melkizedeki wopambana, kumene aneneri opambana akale ndi alembi analemba chotero za iwo. Koma mwa ulesi wawo, mwachithupi, olefuka-pang’ono, osakhala moyo mwaumulungu, Kuwala kwa Uthenga kunali kutachoka.

⁷³ Ndipo apa panali Amitundu, mu mzinda wa Ayuda, akufuula, “Ali kuti Iye amene wabadwa ali Mfumu ya Ayuda? Pakuti ife tawona nyenyezi Yake kum’awa ndipo ife tadza kudzampembedza Iye.” Ndi chinthu chokhudza motani cha tsiku lino, O Atate achifundo, pamene ife tiyang’ana ndi kuganiza! Ayuda anali akugona kufikira amagi, Amitundu akummawa, anachita kubwera kuchokera ku maiko akutali, kuyenda ulendo kuti adzapeze Mfumu ya Ayuda, ndipo iwo sankadziwa kanthu za izo.

⁷⁴ Lero, Mulungu watenga anthu osaphunzira, anyamata ndi asungwana omwe mwina alibe zoposa maphunziro a sukulu ya galamala, wawakweza mwa mphamvu ya Mzimu Woyera, umene ukufuula mmakutu a mpingo, “Iye ali muno mwa mphamvu Yake yopambana, kuti adziwulule Iyemwini ndi kudzizindikiritsa,” ndipo mpingo sukudziwa kanthu za icho.

⁷⁵ Iwo amabwera kudzapereka ulemu. Iwo amabwera kudzapereka ulemu kwa Mfumu ya mafumu. Ndipo mpingo, mu tulo lake la chipembedzo, sukudziwa kanthu za Izo. Iwo ali alendo. Motani, pamene zinyama izi zokondwa bwino, zitakutidwa ndi zoluka zachikale zomwe zimalendewera pa izo, ndi manyenje. Ndipo monga Philon ananenapo, “Iwo sanali mafumu, koma iwo anali—iwo anali otchuka mokwana kuti akhale alendo olemekezeka a Mfumu.” Ndipo ndi awa pano, atakhala pa nsana pa zinyama zolemezekaziki, pamene akudutsa mmisewu, akuti, “Ali kuti Iye amene wabadwa ali Mfumu ya Ayuda?” Baibulo linanena kuti, “Yerusalemu yense ndi Herode nayenso anasautsika.” Umboni wawo unakondoweza chinachake.

⁷⁶ Kodi sizoyipa kwambiri lero, kuti mpingo sungawuke ku kupusa kwake kwa maphunziro a sukulu za ubusa, kuti awone mphamvu ya Khristu wamoyo, wowukitsidwa ndi Ulemerero Wake; monga wosaphunzira, mbuli, chikoka cha chiyanjano cha zipembedzo chikukhudza pa dziko! Bwerani mudzawone Ulemerero wa Mulungu wamoyo. Mzimu Woyera ukugwa chimodzimodzi monga Iwo unachitira pachiyambi. Malemba ayenera kukwaniritsidwa, ndipo pano tiri pamapeto anthawi.

⁷⁷ Ndipo pamene amagi awa ankapitirira akudutsa mu msewu, iwo anakondoweza kuyambira mfumu mpaka mlonda, ndi

uthenga uwu, “Alikuti Iye? Alipati Iye?” Iwo analibe yankho. [M’bale Branham akuwomba mmanja ake kawiri—Mkonzi.]

⁷⁸ Ndipo, lero, pamene ma sputnik akusesa mu mlengalenga, pamene zizindikiro za kuwononga kwathunthu zayandikira; pamene akazi ndi amuna akukhazikika mu tchimmo nakhala mwachikunja, anthu akufuula, “Kodi ichi chikutanthawuza chiyani?” ndipo mpingo ulibe yankho. Iwo ukugona tulo.

⁷⁹ Koma Mzimu Woyera, Kuwala kosafa ndi Kwamuyaya kwa Mulungu, kuli pano kuti kuwalire pa aliyense amene ati alole nakhoza kukulandira Iko.

⁸⁰ Kuwala kunali kutapita. Iwo anali akupereka umboni wawo. Ndipo potsiriza iwo anayitanitsa Sanhedrin palimodzi, ku msonkhano wa bungwe. Ndipo anthu aluntha ndi aneneri analowa mkati, ndi mneneri wamng’ono, mneneri wamng’ono wotsatira, dzina lake Mikaya, uneneri wake. Ndipo iwo anayiwuza mfumu, “Kwalembedwa, ‘Iwe Betelehemu, kodi iwe siuli wamng’ono mwa akalonga onse amu Yudeya? Koma kuchokera kwa iwe kudzabwera kazembe amene adzalamulire anthu Anga, Israeli.’ Chotero, ayenera kukhala Betelehemu kumene Khristu ati adzabadwire, Mfumu ya Ayuda.”

⁸¹ Chabwino, panalibe amene akanawuza iwo momwe angakafikire ku Betelehemu. Koma iwo anatuluka pa chipata, ndipo, pamene iwo anachoka mu mzinda wa mdimawo, Kuwala kunawonekanso patsogolo pawo. Nyenyezi inawoneka. Ndipo Baibulo linati, “Iwo anakondwera ndi chisangalalo chachikulu zedi.” Iwo ayenera kuti anafuula kumene pang’ono. Iwo anakondwera ndi chisangalalo chachikulu zedi. Iwo anali atagonjetsedwa. Iwo...Nyenyezi inawonekera kuti iwatsogolere iwo kumalo awo otsiriza a ulendo wawo.

⁸² Iwo anayitsatira Iyo. Tsopano iwo anayiwona Iyo ikuyandama mmusi koposa momwe Iyo inkachitira. Ili pafupi pang’ono tsopano. Ndipo potsiriza monga...Iwo anapita patsogolo, akusangalala ndi kulemekeza Mulungu, usiku wonse, akutsogozedwa ndi dzanja la Ambuye. Koma potsiriza nyenyeziyo inafika ku khola laling’ono, amene anali malo ang’ono m’mbali mwa phiri, phanga, ndipo kumeneko Nyenyeziyo inakatera pamwamba pa phanga. Ndipo amagi amphamvuwa, atayenda kupitirira chaka ndi miyezi isanu ndi umodzi mu ulendo wawo, ali pa msewu, akuyenda, akuyang’ana, osatsatira kanthu mbali yina ayi koma Nyenyezi. Ndipo pamene Iyo inatera, iwo analowa ndipo mmenemo iwo anapeza mwanayo, Yosefe ndi Maria. Ndipo iwo anabweretsa mphatso kuchokera mu thumba la chuma. Iwo anapereka kwa Iye, golide, lubano, ndi mure.

Ngati ife tikanangokhala ndi nthawi! Tiyeni tiyime kamphindi.

⁸³ Kodi golide ankayimira chiyani? Iye anali Mfumu. Iye sanali woti apangidwe kukhala Mfumu; Iye anabadwa ali Mfumu. Iye anali Mfumu Yamuyaya ya Mulungu. Iye anali Mfumu, kotero iwo anapereka golide.

⁸⁴ Ndipo iwo anapereka lubano. Amenewo ndi mafuta onunkhira, odula kwambiri, opambana amene akanapezeka. Kodi lubano ankanthawuza chiyani, fungo lonunkhira? Iye anali fungo lonunkhira-mokoma kwa Mulungu, pakuti Iye ankapita akuchiritsa odwala namachita zabwino. Golide, chifukwa Iye anali Mfumu. Lubano, chifukwa Iye anali fungo lonunkhira-mokoma kwa Mulungu. Moyo Wake unamkondweretsa Iye kwambiri, mwakuti Mulungu anapuma mu chiyero Chake ndi kukongola, pakuti chinali chiyero Chake Chomwe chikunyezimira mwa Iye.

⁸⁵ O, ngati ife tikanakhala fungo lonunkhira-mokoma, ngati chiyero cha Mulungu chikanakhala chinyezimiro mwa ife; mpaka ife tikhoza kumapita uku ndi uku tikuchita zabwino, monga Yesu waku Nazareti, mpaka ilo kukhala fungo lonunkhira-mokoma kwa Ambuye.

⁸⁶ Koma, ife timakangana, timatsutsana, timapsyetsana mtima, timakayikirana, ndicho chifukwa chake izo zimakhala zonunkha m'mphuno za Mulungu. Miyoyo yathu inali mkati ndi kunja kwa malo akale amene ife sitimayenera kukhalako. Ife timalankhula zinthu zomwe sitiyenera kulankhula. Ife timachita zinthu zomwe sitiyenera kuchita. Ife timakangana ndikutenga mbali ndi dziko, ndi kukana Khristu mu nthawi zopambana kuvuta. Ndicho chifukwa chake ife sitingakhale fungo lonunkhira-mokoma.

Koma, Iye anali, ndipo amagi amenewa anapereka lubano.

⁸⁷ Tsopano iwo anampatsanso Iye mure. Ndipo aliyense amadziwa kuti mure ndi zomera zodula kwambiri koma zowawa. Mure, kodi mure amayimira chiyani? Nsembe Yake yopambana yapamwamba. Moyo Wake wophwanyidwa, waung'ono, pa Kalvare, pamene machimo a m'dziko anamupera Iye mzidutswa. Golide, chifukwa Mfumu. Lubano, wa moyo Wake wokoma, wokonda. Ndipo mure, chifukwa cha nsembe Yake kwa ochimwa, yomwe Iye anafera. “Kumeneko Iye anavulazidwa chifukwa cha zolakwa zathu, natunduzidwa chifukwa cha mphulupulu zathu. Chilango cha mtendere wathu pa Iye, ndipo ndi mikwingwirima Yake ife tinachiritsidwa.” Icho ndi chifukwa chake iwo anampatsa Iye mure.

⁸⁸ Atachenjezedwa ndi Mulungu mu loto, iwo anapita njira yina. Sanabwerere mmbuyo, koma wawo—ulendo wawo unatsirizidwa. Nyenyezi inatsiriza ulendo Wake.

⁸⁹ Kodi nyenyezi imatanthawuza chiyani kwa ife, lero, mzanga? Danieli akutipatsa ife yankho, Danieli 12:3. Akuti, “Iwo amene ali anzeru nadziwa Mulungu wawo adzawala ngati thambo

la kumwamba; ndipo iwo amene atembenezira ochuluka ku chilungamo adzawala ngati nyenyezi ku nthawi za nthawi.”

⁹⁰ Ife ndife chiyani, lero, nanga? Ife ndife nyenyezi. Mkhristu aliyense wobadwanso-kwatsopano ali umboni kwa Ambuye Yesu Khristu, nyenyezi kuti inyezimiritse mphamvu ndi chiyero cha Ambuye Yesu; kuti inyezimiritse Iye mwa Moyo Wake, kumupanga Iye kukhala wangwiro mu malankhulidwe Ake, kumupanga Iye kukhala wangwiro mu mphamvu Yake ya machiritso, kumupanga Iye kukhala wangwiro mu chiwukitsiro Chake, kunyezimiritsa Iye mu njira iriyonse imene Iye ananyezimiritsidwa kwa ife ndi Mulungu Atate. Ife ndife nyenyezi.

⁹¹ Penyani! Kodi inu mukhale nyenyezi ya mtundu wanji? Nyenyezi iyi siyinkatsogoleredwa ndi mphamvu Yake yomwe. Iyo inkatsogozedwa ndi mphamvu zakumwamba za Mulungu Wamphamvuzonse. Ndipo ngati ife titi tikanyezimiritse ochimwa kwa Khristu, ife tiyenera kutsogozedwa ndi Mzimu Woyera. Aroma 8:1, anati, “Palibe kutsutsika chifukwa chache tsopano kwa iwo akukhala mwa Khristu, amene sayenda mwathupi koma mwa Mzimu.” Ngati ife titi tikakhale nyenyezi, kuti tikanyezimiritse Kuwala kwa Khristu, kuti tikabweretse ochimwa kwa Iye, ife tiyenera kutsogozedwa ndi Mzimu Woyera. Kulondola!

⁹² Ndipo ife sitingakhale a wamba. Ife tiyenera kukhala osazolowereka. Ife sitingakhale ozolowereka, chifukwa anthu a Mulungu ndi anthu osamvetseka. Iwo akhala ali, mmibadwo yonse.

⁹³ Ngakhale ali osamvetseka, komabe nyenyeziyo inali yanzeru. Osati yanzeru mwa maphunziro a mdziko, zochitika za mdziko, koma yanzeru monga nsembe pamaso pa Ambuye. Ife timazigoneka tokha, monga amagi anachitira mu Kukhalapo kwa Mfumumu ya mafumu, kukanyezimiritsa Kuwala Kwake.

⁹⁴ Inu ndinu nyenyezi. Mkhristu aliyense ndi nyenyezi, kuti itsogolere otayika, kuti itsogolere olema, phazi la woyenda, kwa iwo amene akufunafuna. Ndiye, nyenyezi siyingadzitsogolere pa yokha, iyo iyenera kutsogozedwa ndi Mzimu. Iyo iyenera kunyezimiritsa nzeru za Mulungu mu moyo wake, kuchoka ku zinthu za mdziko, ndi kukhala moyo waumulungu ndi wofatsa mu moyo unowu. Iyo iyenera kunyezimiritsa Kuwala kwa Mmodzi wopambanayo amene anawala.

⁹⁵ Ndiye ife tizichita chiyano? Kudzuka, ndi kuwonetsa Kuwala kwa Mulungu kwa amene akufa. Mu mdima wakuya wa mdziko lino, ife tiyenera kunyezimiritsa ndi kuwalitsa Kukhalapo kwa Ambuye Yesu mu mphamvu Yake ya chiwukitsiro. Momwe Iye ali dzulo, kotero Iye ali lero, kuti amnyezimiritse Iye.

⁹⁶ Koma kumbukirani, ndiye, Nyenyezi, kachiwiri, pamene iyo yatsiriza ulendo wake, iyo siyimalandira ulemu. Nyenyezi inangowafikitsa amunawo kumalo awo, ndi kuwawonetsa iwo Kuwala kwangwiroko.

⁹⁷ Ndipo ife, monga ziwalo za Thupi la Khristu, mmawa uno, anzanga, ife ndife nyali za Mulungu, koma ife sitimatengera ulemerero kwa ife eni. Pamene ife tikhala ndi chathu—chipiriro chathu, ndi athu—ndi munthu wathu yemwe ife tikumutsogolera; pamene ife tiri nawo, ife tiyenera kusadzipatsa ulemu tokha ndi kuwatsogolera iwo kwa “Kuwala kopambana ndi kwangwiro kumene kumawala, kuti kuwalitse njira ya munthu aliyense yemwe abwera mdziko,” Ambuye Yesu Khristu. Osati nthano yotchedwa Santa Claus, osati mpingo wina mwa chipembedzo; koma Kuwala kowona ndi kwangwiroko, Yesu Khristu, Mwana wa Mulungu wamoyo.

Tiyeni ife tipemphere.

⁹⁸ Mitu yathu titaweramitsira ku fumbi komwe Mulungu anakutengani inu; tsiku lina, mwa kutsimikiza monga momwe nyenyezi zimawala usiku, ndipo dzuwa limawala masana, inu mukubwereranso ku fumbilo. Ngati inu muli pano, pa usiku wa Khrisimasi uwu, ndipo inu mukufuna kukhala ndi Mzimu Woyera kuti ukutsogolereni inu kwa Mpulumutsi, ndi kumulandira Iye motero, kodi inu mungakweze chabe dzanja lanu kwa Iye ndikunena, “Mulungu, mundichitire ine chifundo. Walirani pa njira yanga pamene ine ndikuyenda tsiku lililonse. Ndipo munditsogolere ine, potsiriza, ku Kuwala kwangwiroko, kotero kuti moyo wanga ukhoza kulowererana ndi Wake ndipo ine ndidzakhala ndi Kuwala kwachisavundi Kwamuyaya.”

⁹⁹ Ambuye akudalitseni inu, mlongo wanga wokoneddwa; ndi inu, mlongo wanga; inu, m'bale wanga; inu kumbuyoko, m'bale; ndi inu, mlongo; ndi inu, m'bale wanga. Mulungu akuwona manja anu. O, inu mlongo, Ambuye akukuwonani inu. Inde, chakuno, dona, Ambuye akukuwonani inu, zedi.

¹⁰⁰ “O Yesu, tumizani Mzimu Woyera mmawa uno, tsogolerani moyo wanga wosauka wosocheretsedwa. Ine ndathamanga ndi kujowina mpingo umodzi; ine ndinali wa Katolika, ndipo kenako ine ndinali wa Baptisti, ndipo kenako ine ndinali wa Presbateria. Ine ndinapita kwa Achipentekoste. Ine ndimangopita kulikonse. Ndipo ine ndinafika pozindikira, Ambuye, ine—ine ndimangodabwa; ine sindikudziwa pamene ine ndikuyima. Koma lolani Thupi lakumwambalo, lolani Thunthu lakumwamba la Nyenyezi ya Nthanda, Mzimu wopambana wa Mulungu, unditsogolere ine lero ku malo amenewo mwa Iye komwe ine ndikufuna kukhalako, komwe ine ndikhoza kupanga khola la mtima wanga ndi kumugoneka Ameneyo; kuti Iye akhoze kunditsogolera ine kupyola mmithunzi yonse, mzigwa za

mthunzi wa imfa, kuti ine ndisadzakhale ndi mantha pamene ine ndifika ku njira imeneyo.”

¹⁰¹ Kodi pangakhale wina chabe ndisanatseke? Mulungu akudalitseni inu, bwana; ndi inu, bwana; ndi inu, bwana. Inde, imeneyo inali nthawi yopambana ya munthu, bwana. Kwina kuja ochuluka anali mkazi; nthawi iyi anali amuna amene anayimika manja awo. Zedi, anali amuna anzeru amene anabwera, akufufuza, kutsatira Kuwala. Mulungu akukufunani inu. Wamng’ono Mar- . . .

¹⁰² Maria wamng’ono ndi Yosefe anali atalowa mu mzinda, ndipo kumeneko Yesu anakabadwira. Pa nthawi yomwe amagi anafika, iwo anali akubwera kwa nthawi yayitali, koma potsiriza iwo anafika pachimake chawo chopambana, Nyenyezi inali itawatsogolera iwo. Tsopano inu mwakhala mukufuna kukhala Mkhristu kwa nthawi yaitali, mwina mwatenga ulendo wautali. Apa ndi pachimake mmawa uno, mwina, pakali pano inu mumulandira Iye ngati Mpulumutsi wanu pamene mukumugoneka Iye mu mtima mwanu. Kamodzinsu, tisanatseke kuitanira uku paguwa? Ambuye akudalitseni inu. Zabwino kwambiri. Zikomo inu.

¹⁰³ Ndipo tsopano ndi angati anganene muno, “O Ambuye, monga ine ndawuzidwa ndi Malemba, omwe sangalephere, kuti mu mure uyu amene anaperekedwa kwa Inu, amayimiridwa mmenemo, kutsanula kwa Moyo Wanu. ‘Inu munavulazidwa chifukwa cha zolakwa zathu, ndi mikwingwirima Yanu ife tinachiritsidwa.’ Inu munamva ululu wa kukwapula kowawa pa malo okwapulira, kuti mikwingwirima Yanu ikhoze kutichiza ife. Ine ndikusowa mphamvu Yanu yamachiritso, lero, Ambuye. Mundichotsere mmoyo wanga zokayikira zonse. Chotsani izo kwa ine, kuti ine ndisadzakayikenso. Ndipo ndiroleni ine ndibwere modzichepetsa kwa Inu, tsopano lino, ndi kukhulupirira Inu kwa machiritso anga.”

¹⁰⁴ Mungakweze inu dzanja lanu, kuti, inu anthu odwala? Ambuye apereke pempho lanu, nzanga wokodedwa.

¹⁰⁵ Kodi inu mungamukayikire Iye? Ndithudi ayi. Iye wayima lero ngati Mwana wa Chiwukitsiro kapena . . . ngati—Mwana wa Khrisimasi, Mwana wa Mulungu, Mmodzi wokwanira mu zonse. Iye amakumana ndi chofunikira chirichonse. Iye amakumana ndi chosowa chirichonse chomwe inu mukuchisowa. Mungomulandira Iye. Kodi ife tikuwuzidwa kuti tichite chiyani m’Baibulo? “Kuyika manja pa odwala ndipo iwo adzachiritsidwa.”

¹⁰⁶ Tsopano, Atate Akumwamba, ine ndikubweretsa kwa Inu kagulu aka kakang’ono ka anthu amene Inu mwawatumiza mmawa uno kudzamva Uthenga wa Nyenyezi. Momwe Inu mumachitira ndi munthu wa mayendedwe onse a moyo! Inu mumachita ndi munthu wogulitsa mowa. Inu mumachita ndi

chidakhwa. Inu mumachita ndi wasayansi. Inu mumachita ndi mayi wapanyumba. Inu mumachita ndi mtumiki. Inu mumachita ndi membala wa mpingo. Inu ndinu Mulungu. Inu ndinu wamkulu mwakuti palibe amene angakuthaweni Inu. Ndipo iwo amene ali odzipereka mu mtima wawo, Inu muwonetse chifundo kwa iwo a mafuko onse ndi zikhulupiriro zonse.

¹⁰⁷ Kotero ife tikukuthokozani Inu mmawa uno chifukwa cha iwo amene anakweza manja awo, ena makumi awiri kapena makumi atatu, ine ndikhoza kungoganizira. Ndipo ine ndikupemphera, Mulungu, kuti mphindi yomweyino, tsopano pompa, kuti Kuwala kopambana Kwamuyaya ndi kopanda chivundi kufalikire pa miyoyo yawo, kuti iwo adzapeze mtendere wa lingaliro umene akhala akuwuyembekezera ndi kuwufunafuna, pojowina mipingo ndi—ndi kumachita mipingu yina. Koma Mzimu Woyera uwalire pa iwo.

¹⁰⁸ Monga Yesaya anati, “Anthu awa akukhala mu mdima wokhudzika, koma Kuwala kopambana kwawalira pa iwo.” Perekani, Ambuye, kuti pamenepo uneneri uwu ukhoze kukwaniritsidwa lero mmitima iyi amene akuyembekezera Inu. Perekani kwa iwo mtendere umenewo womwe umapitirira kumvetsa konse, ndi kuwapatsa iwo kukhutitsidwa kwangwiro kuti iwo akomana ndi Inu ndipo alankhula Nanu, ndipo apereka kwa Inu miyoyo yawo, osweka onse ndi osawutsika; kuti Inu, ndi golide Wanu, lubano ndi mure, mukhoze kuwachiza iwo ndi kuwapanga iwo kukhala anthu, zida zolemekezeka kwa ulemerero Wanu Womwe. Perekani izi, Ambuye.

¹⁰⁹ Ndipo tsopano kwa odwala ndi osawutsika, pali dongosolo lomwe Inu mwapatsa ife, kuti ife tizipemphera ndi kuyika manja pa iwo. Ndipo Inu munati, mawu otsiriza amene anagwa kuchokera pa milomo Yanu yopambana, “Mukani inu mdziko lonse ndi kukalalikira Uthenga. Zizindikiro izi zidzawatsata iwo amene akhulupirira; ndipo ngati iwo ayika manja awo pa odwala, iwo adzachiritsidwa.”

¹¹⁰ Ife tikudziwa za mmodzi, msungwana wamng’ono wokondedwa wagona apa, amene wawulusidwa ndi okondedwa okhulupirika kuchokera ku Florida, ndipo iye ali pa siteji yovuta pakali pano. Pamene, ochuluka a antchito Anu apemphera. Ndipo—ndipo adotolo ambiri amuyang’ana ndipo agwedeza mitu yawo, nati, “Sipangakhalenso china chirichonse.” Koma ine ndikuyamika kwambiri kuti mayi wamng’ono, ndi iwo amene akukhudzidwa, sakulola kulitenga ilo ngati yankho. Iwo atsimikiza kuwona kuti mwala uliwonse wagudubuzika. Ngati iwo angangopeza chifundo ndi Mulungu wamoyo, wokondedwa wawo wamng’ono apangidwa kukhala bwino, ndipo iye akhala moyo. O, perekani ichi, Ambuye, palimodzi ndi ena amene ali muno.

¹¹¹ Ambiri ali muno mmawa uno, amene akanakhoza kuyimirira napereka umboni monga amagi anachitira, “Ife tayiwona nyenyezi Yake kummawa.” Ambiri akanakhoza kudzuka nati, “Ife talawapo za ubwino Wake, ndipo ife tamverera mphamvu Yake yamachiritso,” omwe achotsedwa kuchokera mmatupi awo, khansara, ndi maso akhungu, ndi miyendo yopuwala, ndi matenda amitundu yonse. Ndipo ife tikufuula matamando Ake, mwa kukweza liwu lathu, kupyola ku maiko onse, Ambuye.

¹¹² Aloleni iwo, mmawa uno, ana Anu amene akhala muno lero tsopano, akhalenso chimodzimodzi ogawana nawo madalitso Ake. Pamene ife tikuchita ntchito zathu monga atumiki, kupemphera ndi kuyika manja pa iwo, perekani, Ambuye, kuti iwo achiritsidwe mu Dzina la Mwana Wanu, Ambuye Yesu, Yemwe anati, “Pemphani Atate chirichonse mu Dzina Langa, Ine ndidzachichita icho.” Ife tingakayikire bwanji izo, ngati Mulungu ananena izo? Kungokhala zowona monga mauneneri aja a Danieli anayenera kukwaniritsidwa, mowona monga momwe Mulungu akanali moyo, Mawu aliwonse ayenera kukwaniritsidwa. Ndipo ine ndikupemphera kuti Inu mupereke izo kwa ulemerero Wake. Amen.

¹¹³ Ndi mwa chikhulupiriro changa chophweka kwambiri, ndi kutsimikiza ndi kuchita bwino kwa mtima wanga, kuti ngati amuna ndi akazi kuno amene munakweza dzanja lanu kuti mumulandire Ambuye Yesu ngati Mpulumutsi wanuwano... Ine ndikudziwa ndi chizolowezi kuwabweretsa anthu ku guwa. Izo nzolondola. Ine ndiribe chirichonse chotsutsa izo. Koma kubwera ku guwa, inu mukhoza kuchita chinthu chimodzi chokha, icho ndicho, kumuza Mulungu kuti inu muli othokoza kuti Iye anakupulumutsani. Pakuti, miniti yomwe inu mumatanthawuza chimene inu mwanena, pamene inu mukweza manja anu, Mulungu amakulandirani inu chifukwa cha umboni wanu pomwepo. Inu mumanyoza malamulo a mphamvu ya kukokera pansu, ndipo chimodzimodzi monga Nyenyezi imeneyo inanyoza malamulo a zowalitsa mmwamba.

¹¹⁴ Zowalitsa mmwamba zimasuntha mwa njira yake. Ndi momwe izo zimayenera kusuntha. Koma Nyenyezi iyi inanyoza izo, inadutsa pamwamba pa zonsezo, chifukwa Mulungu ndi amene anali kuchita kutsogolera.

¹¹⁵ Lero dongosolo lozolowereka limanena kuti ambiri ainu kuno muyenera kufa. Adokotala achita zonse zomwe iwo akanakhoza kuchita. Izo nzolondola. Koma Mzimu wa Mulungu wamoyo unanyoza zimenezo, unati, “Ine ndikupyoletsa iwe.” Musatero, mwina, sizichitika mu kamphindi. Iwo anapirira, ngati kumuwona Iye amene anali wosawoneka. Abrahamu anapatsidwa lonjezo, ndipo anayembekezera zaka makumi awiri ndi zisanu icho chisanachitike, koma iye ankayendabe natcha chirichonse chosiyana ndi lonjezo ngati kuti panalibe.

116 Ine sindikanakhoza kuyima madzulo a Khrisimasi awa ndi kumalankhula zinthu izi pamaso pa gulu laling'ono la anthu ili ngati ine sindimadziwa kuchokera pa chimene ine ndimalankhulapo.

117 Dzulo, mayi mwina alipo, dzina lawo ndi Akazi a Wright. Kodi inu muli muno, wochokera ku New Albany, Akazi a Wright? Ambiri ainu mukhoza kuwadziwa iwo. Iwo, ine ndikukhulupirira, ndi mayi wodziwika bwino mu New Albany. Msonkhano wotsiriza wamachiritso kuno, kumene... Ine sindimadziwa; zinali mwa kudziwa za mumtima. [Malo opanda kanthu—Mkonzi.]

118 Lamulungu likudzali usiku, Ambuye akalola, ife mwina tikhoza kuyesa kudziwa za mumtima. Ife sitingatenge izo Lamulungu mmawa, chabwino, chifukwa inu munawona Lamulungu lapitali mmawa, monga sabata, chimene chinachitika. Onani, anthu sabwera muno msanga kudzakhala pa mzere, ndi zina zotero, wa mmawa, chifukwa inu muli ndi mbale zoti mutsuke, ndi zina zotero. Koma, Lamulungu usiku, ife tiyesa mwina Lamulungu likudzali usiku, Ambuye akalola.

119 Kudziwa zamumtima kukuchitika, chinthu chimodzi ndikufuna ndichitchule, nditangokuwuzani inu kumene za Akazi a Wright.

120 Iwo sakanakhoza kudzafika kuno. Madokotala aku New Albany, ine ndikhoza kutchula maina awo, koma mwina sichingakhale chanzeru kutero, chifukwa nthawi zambiri iwo samafuna kutero, iwe kuti utero. Ife timayesa kukhala mwamtendere ndi anthu onse, momwe tingathere.

121 Ndipo ife timawakonda madokotala athu. Madokotala, mwina, ali muno mmawa uno. Ine ndiri ndi abwenzi ochuluka madokotala, anthu abwino, anthu Achikhristu omwe amadalira Mulungu. Iwo si achiritso; iwo ndi anthu chabe. Ndipo chimene iwo angathe kuchita, mwathupi, iwo akhoza kuchichita icho. Iwo amangothandizira chirengedwe. Iwo sama... Iwo amakhazikitsa fupa; kuchotsa chotseka, zina ngati zimenezo. Koma Mulungu ayenera kulenga minofu. Mulungu ndi Mmodzi yekha amene angakhoze kuchiza, kapena—kapena kumanga minofu; palibe mankhwala amene angatero.

122 Tsopano, mkazi uyu anali ndi magazi owundana pa mtima wake. Iye anali wa mu zaka makumi asanu ndi limodzi. Iye anatupa moyipa kwambiri mpaka kuti iye anafufuma monga mmene analiri mwawamba. Ndipo iwo anayitana pa foni, ndipo mkazi wanga anandibweretsa ine ku foni, ndipo anati, “Bile, iwo... mkazi akufuna kulankhula nanu, mu New Albany.”

123 Ine ndinati, “Chabwino, mlongo, bwerani, mmawa uno. Ife tikhala ndi msonkhano wa machiritso ku Kachisi uko.”

124 Iye anati, “M'bale wanga wokonedwa,” iye anati, “ine ndikukhumba ndikanamubweretsa iye, koma iye sangathe

nkusuntha komwe.” Ndipo anati, “Iye akufa pakali pano.” Ndipo anati, “Palibe chiyembekezo kwa iye.” Ndipo anati, “Ife tamva za zinthu zopambana zimene Mulungu wachita mwa mapemphero anu. Kodi inu simumupempherera iye? Kodi inu mubwera?”

125 Ine ndinati, “Ine sindingathe kubwera. Koma kodi inu mungayike foni pa khutu lake?”

126 Iye anati, “Ine ndikukhulupirira ndikhoza kusuntha kama lake.” Ndipo iye anasunthira kama lake, ndipo anali naye mkaziyo; sankakhoza nkulankhula komwe.

127 Ine ndinati, “Ngati inu muti mukhulupirire!” Chikhulupiriro ndi thunthu la zinthu zoyembekezeredwa. Osati zimene inu mukungoganiza; koma chomwe inu mukuchidziwa kwenikweni. Chikhulupiriro ndicho. . .

128 Ine ndinati Lamulungu lina, “Ngati ine ndinali ndikufa ndi njala, ndipo ine ndinapempha. . .” Mtanda umodzi wa mkate ukhoza kupulumutsa moyo wanga, ndipo inu nkundipatsa ine 25 tambala; ine ndikhoza kusangalala chimodzimidzi monga ndikanakhala ndi mkatewo, chifukwa pali mikate yambiri.

129 Ndipo pali mphamvu yochuluka yochiza. “Ngati inu simungakhulupirire,” kuti imeneyo ndi 25 tambala; ine ndikhoza kusangalala. Chifukwa, mwina mkatewo uli mailosi khumi kuchokera kwa ine, koma, pamene ine ndapeza 25 tambalayo, chikhulupiriro ndicho thunthu la zinthu zoyembekezeredwa. Ine ndangokhala wokondwa ndi 25 tambalayo ngati kuti ine ndikudya mkate, ngakhale kuti ine ndiri ndi ulendo wautalibe; kudzera mu zigombolera, ndi kuwoloka makhwawa, ndi kuwolokera pa zipika, mpaka mu njira ya minga, ndipo mpaka kukwera phiri. Ine ndikhoza kumvereramverera njala nthawi zonse, mpaka ine kuchita zanzi; ine ndiri ndi njala kwambiri. Koma ine ndizisangalala nthawi zonse, chifukwa ine ndagwirizira 25 tambala, mtengo wa mtanda wa mkate, ziribe kanthu kuti zinthu ziri motani.

130 Abrahamu anasangalala kwa zaka makumi awiri ndi zisanu, atagwiritsitsa chikhulupiriro mu mtima wake kuti Mulungu anali wokhoza kuchita chimene Iye analonjeza. Ndipo iye analandira chimene iye anachipempha.

131 Bwenzi wokonedwa kumeneko, mlongo. Ziribe kanthu kuti pali zochitika zotani, tengani 25 tambalayo, chikhulupiriro chimenecho, c-h-i-k-h-u-l-u-p-i-r-i-r-o. Tengani chimenecho mmanja anu, tengani icho mu mtima wanu, itini, “Palibe kanthu chimene chiti chichitike. . .” Tsopano inu simungadzipangitse-kukhulupirira. Inu muyenera kukhulupirira kwenikweni. “Mwana wanga akhala moyo, chifukwa mu mtima wanga. . . Mulungu wapanga lonjezo, ndipo ine ndiri ndi chikhulupiriro kuti ndikhulupirire izo.” Ndiyeno china chirichonse chimakhala

chotsutsa. Mukuona? Mulungu amachipangitsa icho kusuntha mpaka mu chimenecho—mmalo amenewo.

¹³² Mkazi ameneyo anandiyitana ine dzulo. Ena aiwo anayankha foniyo; iye sanafune kuyitenga iyo. Mkazi wanga anapita ku foniyo; iye sanafune kuyitenga. Iye ankafuna kulankhula ndi ine. Iye anati, “M’bale Branham, ine ndikuyamika dzina lanu.”

Ine ndinati, “Dzina langa? Iwe ukuchitiranji chimenecho?”

Iye anati, “O, ngati inu mukanangondiwona ine!”

Ine ndinati, “Ndiye yamika Mulungu, Iye anali Mmodzi Amene anachita zimenezo.”

¹³³ Iye anati, “Uko madokotala sakutha kupezanso ngakhale kachidutswa ka magari owundana aja. Iko kanamwazikana ndipo kapita. Ndipo ine ndiri bwinobwino, ndikuyenda paliponse mwa thanzi labwino, thanzi labwino kwambiri momwe ine ndinaliri mu zaka.” Dzina lake ndi Akazi a Wright. Iye ali moyo tsopano. . . Iye anandiuza ine dzina lake loyamba. Kwinakwake mu New Albany, ine sindikudziwa pakali pano.

¹³⁴ Mwa kudziwa za mumtima, Lamulungu lapitali, linali sabata, nditayima pano, ndinati, “Ine sindikufuna aliyense wa anthu a m’Kachisi muno. Ine ndikufuna iwo amene siali a m’Kachisi muno. Lolani Mzimu Woyera ulankhule.” Koma mwanjira yina, kumbuyo komwe penapake mbali ina kapena inzake, kumeneko kunali mnyamata wamng’ono dzina lake Hickerson, tonse a ife timamudziwa M’bale Hickerson. Iye ndi chikho chenicheni chowona cha chisomo cha Mulungu. Ndipo iye anawerama mkati mwa anthu ena. Ine sindimamudziwa konse iye. Koma Mzimu Woyera unali utazikonza kale izo zonse. Iye ankayang’ana kupyolera m’nkhwapa mwa munthu wina, atakhala kumbuyoko, ndipo ine sindinkadziwa yemwe iye anali.

¹³⁵ Ndipo ine ndinati, “Mnyamata wamng’ono akuyang’ana pa ine, kupyolera m’nkhwapa mwa munthu uyo. Iye akupempherera wokonedwa wake, ine ndikukhulupirira, mchimwene kapena mulamu, kapena chinachake, amene anali kodwalira amisala; mutu utazungulira, ndipo panalibenso chiyembekezo choti adzakhalanso bwino.” Ndipo Iwo unati, “PAKUTI ATERO AMBUYE. Iye akhala bwino.” Ndipo mnyamata wamng’onoyo anakhulupirira zimenezo, komabe ine sindinadziwe kanthu za izo mpaka patapita masiku.

¹³⁶ Ndipo dzulo iwo anamutulutsa iye ku chipatala cha amisala mu Kentucky, monga, “wangwiwo, abwinobwino, munthu wabwino.” Ndipo mulaliki wathu wamng’ono m’bale wa Methodisti, M’bale Collins, chikho chinanso cha chisomo cha Mulungu. Iye mwina akhoza kukhala ali muno mmawa uno. Onse awiriwo, onse a iwo, mwina ali muno. Anabwera kunyumba yanga usiku wapita, ndi M’bale Palmer wochokera ku Georgia, ndipo amafotokoza kuti mnyamata uyu anadutsa,

pa ulendo wake wopita ku Louisville, atatulutsidwa kuchipatala cha amisalako. Iye wapulumutsidwa, nayenso, ndipo amapita kukakonza zolakwa zake zonse zomwe iye anachita; chikho. Chisomo chosawonongeka cha Mulungu!

¹³⁷ Iye ali yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawi zonse. Musalole mdani kukunamizani inu. Pali Kuwala kosawonongeka kukuwala; Kuwala kosawonongekako ndiko Yesu Khristu, mwana wa Mulungu. Khulupirirani pa Iye. Chikhazikitseni icho mu mtima wanu. Chirandireni icho monga chikhulupiro.

¹³⁸ Tiyeni ife tipemphere ndi kudziwa, kuyika manja pa inu, kukudzozeni inu ndi mafuta, penyani chimene Mulungu adzachite, palibe kanthu kuti pali zochitika ziti.

¹³⁹ Yesu anati, mu Marko 11:24, Iye anati, “Ngati iwe udzanena kwa phiri ili, ‘Zulidwa nuponyedwe mu nyanja,’ ndipo osakayika mu mtima wako, koma kukhulupirira kuti chimene uti unene chidzachtidwa, iwe udzakhala nacho chimene iweyo wanena.”

¹⁴⁰ Tsopano ndiroleni ine ndinene zolembedwa mu lexicon, chimenecho ndicho Chigriki chapachiyambi. Umu ndi momwe zimawerengekera. “Ngati iwe udzanena kwa phiri ili, ‘Nyamuka nuponyedwe mu nyanja,’ ndipo osakayika mu mtima wako, koma kukhulupirira kuti chimene iwe wanena chikwaniritsidwa, ukhoza kukhala nacho chimene wanena.”

¹⁴¹ Pamene iwe wati, “Phiri, lisunthe,” ndipo ilo nkukhalabe pamenepo, iwe nunena, “Chabwino, izo sizinachitike”? O, izo zinachitika. Pamene iwe unati, “Phiri, suntha,” mwina mwala wawung’ono umodzi wosazindikirika wa mchenga unamasuka, pakati pa mazana a mabilioni ndi mabilioni a matani. Mwala umodzi wawung’ono unasuntha, koma izo zikuyamba kuchitika. Gwira chikhulupiro chimenecho ndipo uliwone phiri limenelo likuchoka. Ndithudi.

¹⁴² Inu mudzati mu mtima wanu, “Nthenda, choka pa mwana wanga. Nthenda, choka pa thupi langa, mu Dzina la Ambuye Yesu,” ndipo osakayika. Pomwepo majeremusi abwino amatenga chida chatsopano ndi chipangizo chatsopano, ndipo mdani amayamba kubwerera mmbuyo. Iye wagonjetsedwa chifukwa Khristu, pakumwa kwa mure Wake pa Kalvari, anagonjetsa Mdierekezi ndi imodzi iliyonse ya mphamvu zake. Ndipo Iye anamuvula mdierekezi chirichonse chimene iye anali nacho, ndipo iye siali kanthu koma chongowopyseza; iye akhoza kupyola nacho icho, iye achichita.

¹⁴³ Ife tatsimikiza, mwa chisomo cha Mulungu, kukalalikira Uthenga ndi kunyezimiritsa Kuwala Kwake mpaka Iye atadza.

¹⁴⁴ Tsopano, Ambuye, zinazo ziri kwa Inu. Ife tsopano tiwayitana anthu awa, ndipo Mzimu Woyera ubwere Mkachisi wamng’ono uyu ndi kudzapanga chikhulupiro mu mtima uliwonse, pamene iwo akuyima ndi kubwera cha kuno kuti adzapempheredwe. Mulole iwo achoke lero nachita

monga amuna anzeru aja; pamene iwo anawona Nyenyezi kachiwiri, itatha nthawi ya mdima, iwo anakondwa ndi chisangalalo chopitirira kupambana; ndipo anthu awa, pamene adzozedwa ndi kupemphereredwa. Yakobo anati, mu Uthenga, “Itanani akulu a mpingo ndipo awadzoze iwo ndi mafuta ndi kuwapempherera iwo. Pemphero la chikhulupiriro lidzapulumutsa odwala.” Mulole anthu akondwe ndi chisangalalo chopambana kopitirira, podziwa kuti chikhulupiriro cha Mulungu chafalikira mmitima yawo, ndipo iwo adzakhala nazo zomwe iwo afunsa.

¹⁴⁵ Tsopano, Atate, Inu mwachita gawo Lanu. Ine ndachita zonse zomwe ine ndimazidziwa kachitidwe kake, kupatula kuyika manja pa anthu ndikuwadzoza iwo. Tsopano zotsalazo ndi za iwowo. Mulole kuti zisalephereke. Mulole kuti gudumu lirilonse la wotchi yosafa ya Mulungu liyende mwangwiro mmawa uno, pamene odwala akudzozedwa. Chifukwa cha Yesu Khristu ife tikupempha izo, mu Dzina Lake. Amen.

Ngati inu mutangokhulupirira,
kungokhulupirira chabe,
Zinthu zonse ndizotheka, kungo. . .

¹⁴⁶ Momwe nyimbo imeneyo imachitira chinachake kwa ine! Zilankhulo mazana. . . ine ndamvapo achikunj a ndi Akafula akuyimba imeneyo pamene ine ndinali kubwera pa msanja.

¹⁴⁷ Mkazi yemwe uyu, wa limba yemweyo, momwe ine ndikudziwira, anaphunzitsa nyimboyo kwa ine, zaka khumi ndi chimodzi zapitazo, ine ndisanachoke mu utumiki. Paul Rader, bwenzi langa, anailemba iyo.

¹⁴⁸ Yesu, akutsika kuchokera ku phiri, Iye anawona mnyamata ali ndi khunyu. Ophunzira sanathe kuchita kalikonse nalo. Iye anati, “Ambuye, Mchitireni chifundo mwana wanga.”

¹⁴⁹ Iye anati, “Ine ndikhoza ngati inu muti mukhulupirire, pakuti zinthu zonse ndi zotheka; kungokhulupirira.” Pamenepo ndi pomwe Paul anapezera zolemba zake, *Kungokhulupirira*. “O- . . .”

¹⁵⁰ Tsopano penyani kutali kuchoka ku matenda anu tsopano. “Ingokhulu- . . .” Kodi inu simungachite zimenezo? “Zinthu zonse ndi zotheka, ingo. . .”

¹⁵¹ Tangokumbukirani, Iye wayima pano. Iye ndi wokondeka. Iye analonjeza izo. Iye akunyezimiritsa zowala Zake; tawaonani ena akuchiritsidwa. Zedi, inu mukhoza, nanunso. “Tapenyani kwa ine,” munthu wakhungu wochizidwa, mukuona. Tawapenyani kwa ena, tangopenyani momwe, mai, chomwe Ambuye wachita! “. . . zotheka. . .”

¹⁵² Ndi angati akukhulupirira zimenezo pakali pano inu muli ndi chikhulupiriro mu mtima mwanu chonena kuti, “Ine ndikukhulupirira chakhazikika. Ine ndikukhulupirira ndikhoza

kumulandira Iye tsopano pompa. Ine ndikukhulupirira ndikhoza kunena kuti ndikhala bwino. Ziribe kanthu kaya chichitika chiyani, ine ndikunena kwa phiri ili la matenda, ‘Chotsedwa ndi kundisiya ine, kapena okonedwa anga, kapena aliyense amene ali.’ Ndipo ine ndikukhulupirira kuti icho chidzachitika?”

¹⁵³ Muwone chimene chiti chichitike. Matenda amenewo ayamba kuphwasuka. Iwo ayamba kusuntha. Chinthu choyamba inu mukudziwa, adokotala adzati, “Chachitika ndi chiyani apa?” Izo nzolondola, ngati inu mungakhulupirire.

¹⁵⁴ Kodi inu mungabwere, M’bale Neville? Tsopano aloleni iwo amene ali mu mzere uwu *pano*, ayimire mbali *iyi*. Ndipo inu amene muli mu mzere *uwu*, muzungulire kumbuyo ndipo mubwere chozungulira, ngati inu mungafune, koteri ife tikhoza kukhala ndi mzere umodzi. Ife tikufuna akulu a mpingo abwere kutsogolo, kuti adzayime nawo anthu, pamene iwo akupemphereredwa.

¹⁵⁵ Tsopano, msungwana wamng’ono, ife titsika ndi kudzampempherera mwana wamng’ono wagona apayu. Ife tingobwera pomwepo pamene iye ali.

¹⁵⁶ Ine ndikufuna iwo amene . . . ena amene ati apemphereredwe, apite ku mbali iyi tsopano. Ine ndikufuna munthu aliyense muno kuti akhale mu pemphero pakali pano. Inu muli ndi gawo lochita nawo izi. Othandizira atayima kumeneko akutsogolerani inu mu mzere umene inu muyenera kufolamo pa nthawi ino.

Zinthu zonse ndi zotheka, kungokhulupira.

Musaope, nkhosa zochepa, kuchokera ku mtanda mpaka ku mpando wachifumu, Kuchokera ku imfa kumka ku moyo Iye anapita chifukwa cha Ake omwe;

Mphamvu zonse panso pano, mphamvu zonse m’mwamba,

Zinapatsidwa kwa Iye chifukwa cha nkhosa za chikondi Chake.

Nyenyezi ya Khristimasi ikuti chiyani tsopano?

Kungokhulupira, kungokhulupira,

Zinthu zonse ndizotheka, kungokhulupira;

Kungokhulupira, kungokhulupira,

Zinthu zonse ndizotheka, kungokhulupira.

¹⁵⁷ Anzanga okonedwa, alipo ambiri muno amene akukupemphererani tsopano; amuna abwino ndi akazi abwino, oyera mtima, amuna ndi akazi a umulungu.

¹⁵⁸ M’bale wanga Neville akuyima pano pambali yanga, amene ine ndamudziwa kwa zaka kuti ndi munthu waumulungu. Anthu amene amabwera kuno kuchokera kunjira kwa mzinda, iwo anandiyitana ine pa foni, anati, “Ndi ndani munthu uja amene ali m’busa wanu? Ndipatseni ine adiresi yake; ine ndikufuna

kumulemba iye. Iye akuwoneka ngati munthu woona mtima.” Ine ndiri wokondwa kuti ndikhoza kunena, “ndiponso mmodzi wa anthu aumulungu kwambiri omwe ine ndikuwadziwa.” Iye amakhala moyo chimene amalalikira ndi chomwe amalankhula. Iye ali ndi mafuta odzozera mdzanja lake.

Mulungu ali ndi mphamvu mdzanja Lake.

¹⁵⁹ Kodi inu muli ndi chikhulupiriro mu mtima wanu? Ngati inu muli nacho, ichi chiyenera kuchitika. Kunjako chakuno, kuno kuli atumiki, anthu aumulungu ali kuno akhala akukupemphererani inu. Chinachake chiyenera kuchitika tsopano.

¹⁶⁰ Chinachake chakufikitsani inu patali chonchi; iyo inali Nyenyezi, tsopano, Nyenyezi, Nyenyezi ya Nthanda. Tsopano landirani kwa chisavundi, Kuwala Kwamuyaya. Monga inu chabe, ife tikutsatira kachitidwe aka, monga kukubatzani inu, kapena chirichonse, mukuona. “Kuwadzoza odwala m’mafuta, kupempherera pa iwo; pemphero la chikhulupiriro lidzapulumutsa odwala.”

¹⁶¹ Yesu anati, mawu otsiriza kwa Mpingo Wake, “Zizindikiro izi zidzawatsata iwo amene akhulupirira; iwo adzaika manja awo pa odwala, iwo adzachiritsidwa.” Mwakulankhula kwina, ine ndikhoza kunena ichi, kuziyika izo mwa mawu omwe mukuwadziwa, “Kulikonse kumene Uthenga uwu walalikidwa, mdziko lonse, antchito Anga adzayika manja pa odwala, iwo adzakhala bwino.” Chabwino. Mukuona?

¹⁶² Tsopano pali chinthu chimodzi chokha choti chitsutse zimenezo, ndicho, kusakhulupirira. Inu mukuona, izo sizikuyika...ngakhale ngati-ngati m’bale ndi ine tinali... sitinali oyenera konse kulalikira Uthenga; zomwe, ife sitili, mwa chisomo Chake chokha. Koma, palibe kanthu chomwe ife tikanakhala, ndi Mawu Ake. Iye, Iye sasowa kukanirira kwa ife, koma Iye ayenera kukhala mwa Mawu Ake, “Ngati inu mungakhulupirire.”

¹⁶³ Tsopano ndi angati kunjako mwa omvera ati akhale akupempherera anthu amenewa? Kwezani manja anu. Ine ndikufuna anthu inu muyang’ane kunjika uko. Kumeneko ndi komwe mapemphero akupita, kumka Kumwamba chifukwa cha inu tsopano. Tsopano mutu uliwonse utawelama ndipo aliyense akupemphera, pamene m’bale akudzoza.

¹⁶⁴ Kaminiti kokha tsopano, ife tikhala ndi pemphero lapagulu kwa awa pano.

¹⁶⁵ Ambuye wachifundo, ife tikupita patsogolo tsopano monga antchito Anu, kukachita ntchito ya atumiki. Muli ambiri muno, Ambuye, mu mzere, amene ali kwambiri, kudwala kwambiri, mopanda kukayika. Ena a iwo ali pafupi kufa. Ndipo ena aiwo ali pa mipando yawo. Monga mwachitsanzo, msungwana wamng’ono amene wachokera ku Florida. Pali ena muno

ochokera ku Georgia ndi ochokera ku malo osiyana, ochokera mpaka ku Indianapolis, ena ochokera ku Ohio, asonkhana mu gulu laling'ono ili mmawa uno, akhala akuyembekezera kuno mu mahotelo ndi chirichonse, kuyembekezera ora la kuti apemphereredwe. Iwo akhala ali mu misonkhano. Iwo awona dzanja Lanu likuyenda nilichita ntchito. Ndipo pomwe pano tsopano... Ambuye, chotsani nthano za Santa Claus ndipo bweretsani kwa iwo mphatso yeniyeni ya Khristimasi. Apatсени iwo thanzi labwino pakali pano, Ambuye, chifukwa iwo abwera akukhulupirira.

¹⁶⁶ Ndipo ife tikubwera, kuyima pakati pa iwo ndi Ambuye Mulungu Wakumwamba, kuwapangira iwo chitetezero, kupemphera ndi kupereka zolankhula za mawu athu omwe, mmalo mwa iwo. Mulole mmodzi wa iwo, Ambuye, asalephere kukhala ndi chikhulupiriro.

¹⁶⁷ Ife tikudziwa Mawu amanena zimenezo. Ife tikudziwa kuti ife timakhulupirira zimenezo. Tsopano, Ambuye, mulole iwo akhulupirire izo ndi kulandira chimene iwo apempha. Ife tikupita patsogolo tsopano monga akazembe a Khristu, ndi thupi lonseli la mpingo, kupemphera mwa umodzi kuti iwo achire. Mulole zikhale choncho. Ndipo pamene iwo azichoka, mulole iwo apite ndi chisangalalo chachikulu mopitirira chifukwa—M'bandakucha wadza pa ife. Zowala zazikulu za Kumwamba zatembenukira ku njira yathu, ndipo ife tikumuwona Ambuye Yesu wowukitsidwa mu Mphamvu Yake ndi Ulemerero. Amen.

¹⁶⁸ Pamene iye akudzozedwa, mu Dzina la Ambuye Yesu, ife tikuyika manja pa iye, ndi kupempha kuti matenda ake achiritsidwe ndi dzanja la Mulungu Wamphamvuzonse, mu Dzina la Yesu. Amen.

¹⁶⁹ Mulungu akudalitse iwe. Pita ndipo ukalandire iwo, mu Dzina la Ambuye Yesu.

¹⁷⁰ Pokhala atadzozedwa, mu Dzina la Ambuye Yesu, ife tikupempha chokhumba cha mtima wake chiperekedwe, mu Dzina la Ambuye Yesu.

¹⁷¹ Monga pokhala atadzozedwa ndi mafuta, ife tikuyika manja pa m'bale wathu, mu Dzina . . .



KUWALA KWAKUKURU CHA57-1222
(The Great Shining Light)

Uthenga uwu wa M'bale William Marrion Branham, woperekedwa mu Chingerezi Lamlungu mmawa, pa 22 Disembala, 1957, ku Branham Tabernacle mu Jeffersonville, Indiana, U.S.A., unatengedwa kuchokera pa matepi ojambulidwa ndi maginito nudindidwa mosachotsera mawu ena mu Chingerezi. Kumasulira kwa Chichewa uku kunadindidwa ndi kugawidwa ndi Voice Of God Recordings.

CHICHEWA

©1992 VGR, ALL RIGHTS RESERVED

VOICE OF GOD RECORDINGS, MALAWI OFFICE
P.O. BOX 51453, LIMBE, MALAWI

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. BOX 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.
www.branham.org

Chidziwitso kwa ofuna kusindikiza

Maufulu onse ndi osungidwa. Bukhu ili mukhoza ku printa kunyumba kwanu ngati mutafuna kuti mugwiritse ntchito inuyo kapena kuti mukawapatse ena, ulere, ngati chida chofalitsira Uthenga wa Yesu Khristu. Bukhu ili simungathe kuligulitsa, kulichulukitsa kuti akhalepo ambiri, kuikidwa pa intaneti, kukaliika pakuti ena azitengapo, kumasuliridwa mu zinenero zina, kapena kugwiritsidwa ntchito ngati njira yopezera ndalama popanda chilolezo chochita kulembedwa ndi a Voice Of God Recordings®.

Ngati mukufuna kuti mumve zambiri kapena ngati mukufuna zipangizo zina zimene tiri nazo, chonde mulembere ku:

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. BOX 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.
www.branham.org